

MALAMULO KHUMI.

Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha. 2. Usadzipangire iwe wekha fano losema. 3. Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe. 4. Uzikumbukira tsiku la Sabata. 5. Uzilemekeza atate wako ndi amako. 6. Usaphe. 7. Usachite chigololo. 8. Usabe. 9. Usanamizire mnzako. 10. Usasirire. Mudzawonana ndi Mulungu pa tsiku la chiweruzo. Iye awona kusirira monga kuchita chigololo. “Koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wakuyang’ana mkazi ndi kumkhumba, pamenepo watha kuchita naye chigololo mumtima mwake.” (Mateyu 5:28). Iye awona udani monga kupha. “Yense wakudana ndi m’bale wache ali wakupha munthu” (1 Yohane 3:15). Kodi mudzalowa Kumwamba? Nawa mayeso a pafupi. Kodi munanenapo bodza, kuba chinthu, kugwiritsa ntchito dzina la Mulungu pachabe, kapena kuyang’ana mosilira. (Yakobo 2:10) akuti, “Pakuti amene aliyense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi iyeyu wachimwira onse.” Kodi simudzakhala akuchimwira pa tsiku la chiweruzo. Ngati munachitapo zinthu zimenezi Mulungu amakuonana onama, akuba, amwano, achigololo. Buku Lopatulika likutichenjeza ife kuti ngati tili ochimwa mapeto athu akakhala ku Gahena. Mulungu anatuma Mwana Wake kuti avutike ndi kufa pa mtanda. Yesu anadzitengera chilango yekha, “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha, kuti aliyense wakukhulupirira mwa Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha.” (Yohane 3:16). Yesu anauka kwa akufa nagonjetsa imfa. Lapani (tembenukani ku machimo anu) lero ndi kukhulupirira mwa Yesu, ndipo Mulungu adzakupatsani moyo wosatha. Werengani Buku Lopatulika ndi kutsatira zomwe mumawerenga.

MAWU A MULUNGU I

Musoweka kupulumutsidwa. “Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu.” Tonse tasochera ngati nkhosa; tonse tayenda yense mnjira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse. (Yesaya 53:6). Ine Yehova ndisanthula mtima ndiyesa imso, kuti ndimpatse munthu yense monga mwa njira zache, monga zipatso za ntchito zache. (Yeremiya 17:10). Ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo. (Luka 13:3). Simungadzipulumutse nokha. Mulungu anatipulumutsa ife, zosati zochokera ntchito za mchilungamo, zimene tidzachita ife, komatu monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera. (Tito 3:5). Iripo njira yowoneka kwa munthu aliyense ngati yowongoka; koma matsiriziro ache ndi njira za imfa. (Miyambo 14:12). Yesu ananena naye, Ine ndine njira ndi choonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine (Yohane 14:6). Palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo. Zimangotiwunikira kuti ndife ochimwa (Aroma 3:20). Mulungu anaikiratu chipulumutso. Yesu anasenza machimo athu pa mtanda kuti tikhale akufa ku uchimo ndi kukhala ndi moyo kutsata chilungamo. Ndi mikwingwirima yake tinachiritsidwa (1 Petro 2:24). Yesu anafera machimo athu, ndipo tsiku lachitatu anauka kwa akufa (1 Akorinto 15:3-4). Muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro. Ichi chosachokera kwa inu. Chiri mphatso ya Mulungu. Chosachokera ku ntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense. (Aefeso 2:8-9).

MAWU A MULUNGU II

Khulupirirani Mau a Mulungu ndipo mudzapulumuka. Yesu anayankha nati kwa iwo, “Ntchito ya Mulungu ndi iyi, kuti mukhulupirire Iye amene Iyeyo anamtuma. (Yohane 6:29). Indetu, indetu ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi khulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nawo moyo wosatha, ndipo salowa mkuweruza koma wachokera ku imfa nalowa mmoyo (Yohane 5:24). Iye wakukhala ndi Mwana ali nao moyo, wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo. Izi ndakulemberani kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu (1 Yohane 5:12-13). Vomerezani Yesu pamaso pa anthu. Amene aliyense adzachita manyazi chifukwa cha Ine ndi mau anga, Mwana wa munthu adzachita manyazi chifukwa cha iye (Luka 9:26). Ngati udzavomereza mkamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa udzapulumuka. Pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo chilungamo, ndi mkamwa avomereza kutengapo chipulumutso (Aroma 10:9-10).

Chikhulupiliro chopanda ntchito zache chikhala chopanda pache. Phindu lake ndi chiyani, abale anga, munthu akanena, Ndiri nacho chikhulupiro koma alibe ntchito? (Yakobo 2:14). Pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe chifukwa cha kukoma mtima kwache, ndiye Mulungu. (Afilipi 2:13). Munthu aliyense wa ife adzadziwerengera mlandu wache kwa Mulungu. (Aroma 14:12). Koma ngati kutumikira Yehova kukuipirani mudzisankhire lero amene mudzamtumikira. Komai ne dni a mnyumba yanga tidzatumikira Yehova (Yoswa 24:15).

CHIKONZERO CHA MULUNGU CHA CHIPULUMUTSO I

Funso lofunikira kwambiri mmoyo wanu ndi lakuti kodi mudzapita kumwamba mukadzafa? Mulungu akunena kuti mukalowe kumwamba, “Muyenera kubadwanso” (Yohane 3:17). Mu Buku Lopatulika, Mulungu anapereka chikonzero cha kubadwanso. Choyamba, zindikirani kuti ndinu wochimwa. “Pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemmero wa Mulungu” (Aroma 3:23). Pakuti ndinu wochimwa, muyenera kulandira imfa. “Mphotho yache ya uchimo ndi imfa” (Aroma 6:23). Izi zitanthauza kuti kulekana kwa muyaya ndi Mulungu, kukhala ku Gehena. “Popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa chiweruziro. (Ahebri 9:27). Koma Mulungu anakukondani kwambiri anapereka Mwana wake wobadwa yekha, Yesu, kusenza machimo ndi kufa mmalo mwanu. “Koma Mulungu anatsimikiza kwa ife chikondi chake pakutumiza Khristu kuti pokhala ife chikhaliwe ochimwa Khristu anatifera.” (Aroma 5:8). Ngakhale sititha kumvetsetsa mmene Mulungu anati machimo athu anaikidwa pa Yesu kuti lye anafa mmalo mwathu. “Mulungu akulamula anthu onseponseponse atembenuke mtima. (Machitidwe 17:30). Kulapa kutanthauza kutembenuka kuchoka ku machimo anu ndi kuvomereza pamaso pa Mulungu kuti ndinu wochimwa, ndi kuvomereza zimene Yesu anatichitira pa mtanda. Funso: “Kodi ndichite chiyani kuti ndipulumuke?” (Machitidwe 16:30). Yankho: Khulupirirani mwa Yesu monga amene anasenza machimo anu, anafa mwalo mwanu, anaikidwa mmanda, amene Mulungu anamuikitsa kwa akufa. Kuuka kwake kumatitsimikizira ife kuti tikalandire moyo wosatha pamene mulandira Yesu monga Mpulumutsi wanu. “Koma onse amene anamlandira lye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu. (Yohane 1:12).

CHIKONZERO CHA MULUNGU CHA CHIPULUMUTSO II

“Aliyense amene adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka (Aroma 10:13). Khulupirirani, ndipo mudzapulumuka. Simudzapulumuka chifukwa cha mpingo kapena ntchito zabwino. Kumbukirani, Mulungu ndiye amene amapulumutsa. Chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso ndi: Inu ndinu wochimwa ndipo ndi pokhapokha mwalapa ndi kukhulupirira mwa Yesu amene anafa mmalo mwanu, apo ayi mukakhala kwa muyaya ku Gahena. Ngati mukhulupirira pa lye monga wopachikidwa, woikidwa mmanda ndi Mpulumutsi wa moyo, mudzalandira chikhululukiro cha machimo anu onse ndi kulandira mphatso ya moyo wosatha mwa chikhulupiro. Ngati simukumvetsetsa chikonzero cha Mulungu, muwerenge mobwereza musanaike papalali pansu kufikira mutamvetsetsa. Moyo wanu ndi wofunikira kwambiri kuposa dziko lapansi. “Munthu apindulanji akadzilemezera dziko lonse natayapo moyo wache.”(Marko 8:36). Onetsetsani kuti mupulumutsidwe. Mukataya moyo wanu, musemphana ndi kumwamba ndiponso mutaya zonse. Musakhulupirire maganizo anu chifukwa amasintha. Imani nji pa malonjezo a Mulungu amene sasintha. Mukapulumutsidwa, pali zinthu z tatu zimene muyenera kuzizolowera mmoyo wanu wa uzimu tsiku ndi tsiku. Choyamba ndicho kupemphera, kumene kuli kulankhulana ndi Mulungu. Chachiwiri ndi kuwerenga Buku Lopatulika kuti Mulungu alankhule nanu. Chomalizira ndicho kugawana ndi anzanu za chikhulupiro chanu kuti mukhale cholankhulira cha Mulungu. “Usachite manyazai pa umboni wa Ambuye wathu”(2 Timoteo 1:8). “Yense amene adzavomereza lne pamaso pa anthu, Inenso ndidzamvomereza iye pamaso pa Atate wanga wa Kumwamba. (Mateyu 10:32). Muyenera kubatizidwa kuonetsa kutsatira Ambuye Yesu Khristu, monga umboni wa chipulumutso kwa anzanu, ndi kukhala pamodzi ndi anzanu a mpingo okhulupirira Buku Lopatulika.